Maphunziro

a

Alangizi othandizira alimi a ziweto m'midzi

Katemera woteteza ku matenda a chideru

Small Scale Livestock and Livelihoods Program
PO Box 1604, Lilongwe Malawi

Katemera woteteza ku matenda a chideru

Illustration courtesy of Kyeema Foundation

Phunziro 1: Zokhudza matenda a chideru

Zolinga za phunziroli:

Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe:

1. **Kudziwa kufunika kwake kwa matenda a chideru mokhudzana ndi nkhuku za m'midzi muno m'malawi**
2. **Kudziwa zizindikiro za nkhuku yomwe ikudwala matenda a chideru**
3. **Kumvetsa kufunikira kotemera nkhuku pofuna kuziteteza ku matenda a chideru**
4. **Kumvetsa kusiyana kochiritsa nkhuku kumatenda ndi kuteteza nkhuku ku matenda**
5. **Kudziwa kuti palibe mankhwala ochizira matenda a chideru**

Kodi matenda achideru ndi wotani?

- Matenda a chideru (maina ena ndi "chitopa" kapena "dzowe") ndi matenda amene amapha nkhuku zambiri ndiponso kudwalitsa nkhuku zambiri.
- Matenda a chideru amagwa panthawi ndi kupha nkhuku zambiri ndipo amapita kwa miyezi ingapo asanagwenso. Alimi akumidzi amadziwa za m'mene matendawa amagwera.

Kodi chimayambitsa matenda a chideru ndi chiyani?

- Matenda a chideru kamayambitsa ndi kachirombo ka mtundu wa vairasi. Kachiromboka kamafala ndi nkhuku zodwala, mbalame ngakhale anthu amene agwira nkhuku zodwala chideru.

Kodi kuopsa kwa matenda a chideru ndi kotani?



- Matenda a chideru ndi oopsa **kwambiri**. Ndi matenda amene amapha nkhuku zambiri muno m'Malawi.
- Matenda ena ogwira nkhuku atha kupha nkhuku koma sangafanane ndi m'mene matenda a chideru amaphera nkhuku.

Nanga nkhuku yodwala matenda a chideru imaonetsa zizindikiro ziti?

- Matenda a chitopa amagwira zigawo za bongo, mapapo ndi matumbo a nkhuku.

  - Ngati tiziromboti tagwira m'bongo, nkhuku zimapinda khosi kapena kumazungulira pamodzimodzi kapena kumangogwa.

  - Ngati tiziromboti tagwira m'mapapo, nkhuku zimatsokomola kapena kuyetsemula ndi kumachita mamina.

  - Ngati tiziromboti tagwira m'matumbo, nkhuku zimanyera chitosi cha mpwerere chamtundu wobiriwira.

- Nthawi zina matendawa akalowa m'khola, amatha kupha nkhuku zonse. Koma nthawi zina amatha kupha nkhuku zochepa koma zimatha kudwala zonse.

Kodi tikhoza kuchiza matenda a chideru motani?

- Kuchiza ndi kuteteza matenda ndi zinthu ziwiri zosiyana.
  - Kupereka mankhwala kumachiza matenda omwe chiweto chayamba kale kudwala
  - Kuteteza ndi pamene tafuna kuti chiweto chisagwidwe matenda ngakhale tizirombo toyambitsa matendawo talowa m'thupi lachiweto.
- Dziwani kuti palibe mankhwala ochizira matenda a chideru. Ngati matendawa agwa m'khola yembekezerani kuti nkhuku zambiri zifa ndithu.
- Ngati wina akanena kuti ali ndi zitsamba kapena mankhwala ochizira matenda a chideru akungokunamizani.

Nanga tikhoza kuteteza nkhuku kumatenda a chideru motani?

- Njira yeniyeni yotetezera nkhuku ku matenda a chideru ndi kutemera nkhuku zonse. Kutemera nkhuku sikovuta ayi ndipo sikokwera mtengo.
- Ku maiko ena alimi amateteza nkhuku ku matenda a chideru popatula nkhuku zawo kuti zisakumane ndi nkhuku zina. Koma kuno ku Malawi ndi zosatheka kupatula nkhuku za m'midzi chifukwa zimakumana kunja pofuna zakudya.

Phunziro 2: Katemera woteteza matenda a chideru ku nkhuku

Zolinga za phunziroli:

Pomaliza pa phunziro ili wophunzira athe:

1. **Kumvetsetsa za m'mene katemera amagwirira ntchito m'thupi la chiweto**
2. **Kutemera nkhuku mosavuta**
3. **Kuyankha mafunso okhudza katemera woteteza nkhuku ku matenda a chideru**

- Ngati kachirombo koyambitsa matenda a chideru kalowa m'thupi la nkhuku, nkhuku imayamba kudwala patapita tsiku limodzi. Nkhuku imafa tsiku lotsatilalo. Ngati nkhuku siifa tsiku latsatilalo ndipo ikachira, ndiye kuti thupi lake lapanga asilikali ogonjetsa matendawa. Kupanga asilikali oteteza kumachitika mkati mwa mulungu umodzi. Ngati nkhuku yotereyi igwidwanso ndi matendawa, asilikali achitetezo a m'thupi aja amaononga tizirombo toyambitsa matenda tija mwamsanga ndipo nkhuku sidwala ayi.
- Katemera amapanga asilikali omenyana ndi tizirombo toyambitsa matendawa pokhapokha ngati nkhuku zisanayambe kudwala matendawa. Nkhuku zimakhala ndi chitetezo champhamvu ku matenda. Nkhuku yotemeredwa sidwala ngati kachirombo koyambitsa matenda a chideru kakalowa m'thupi lake.
- Katemera amatenga mulungu umodzi kuti apange chitetezo chokwana m'thupi la nkhuku. Ndipo ngati nkhuku yatemeredwa itayamba kale kudwala matenda a chideru, ikufa ndithu, katemera asanapange chitetezo chokwana.
- Choncho ntchito ya katemera ndi kuteteza osati kuchiza matenda a chideru.
  - Ngati nkhuku yalandira katemera pa tsiku lomwe yayamba kudwala matenda a chideru, ikhoza kufa ndithu.
  - Ngati nkhuku yalandira katemera ili kale ndi matenda a chideru m'thupi lake, ikhoza kufa ndithu.
  - Ngati matenda a chideru agwira nkhuku patapita mulungu umodzi zitalandira katemera, singathe kudwala.
- Mphamvu za chitetezo zimayamba kutsoka m'thupi lankhuku yomwe inalandira katemera pakatha miyezi inayi ndiye ndikoyenera kutemeranso nkhuku zanu.
  - **Bwerezani kutemera nkhuku zanu pa miyezi inayi ili yonse.**
- Katemera woteteza matenda a chideru amateteza matenda a chideru okha osati matenda ena ayi. Choncho nkhuku zomwe zalandira katemera

woteteza matenda achideru zitha kugwidwa ndi kufa ndi matenda a mtundu wina omwe amagwira nkhuku.

- Katemera woteteza ku matenda a chideru sioopsa ayi. Ngati nkhuku zidwala kapena kufa zitangolandira katemerayu ndiye kuti zadwala ndi kufa ndi matenda ena osati katemerayu.
- Katemera woteteza ku matenda a chideru sioopsa ayi. Sasintha kaonekedwe ndi kakomedwe ka nyama ya nkhuku ayi.
- Osatemera nkhuku zimene zili kudwala. Temerani nkhuku zomwe zili za thanzi matenda asanagwe m'mudzi.
- Ngati mutemera nkhuku zimene zili kudwala, katemerayo sagwira ntchito ayi.
- Ngati mutemera nkhuku zoti zili kudwala, choti mudziwe zikufabe basi. Ngati zitero, mlimi mwini nkhuku amaganiza kuti nkhuku zafa chifukwa cha katemerayo ndipo savomera kuti nkhuku zake zilandire katemera mtsogolo. Nkhuku zake zimakhala zosatetezedwa.
- Pali mitundu yosiyanasiyana ya katemera woteteza nkhuku ku matenda a chideru. Pano tikamba za mtundu wa katemera wotchedwa I-2 amene akupezeka muno m'Malawi ndipo ndiwabwino kugwiritsa ntchito ku mudzi.

Kasungidwe ka katemera wotchedwa I-2

- Musaziriritse katemera ameneyu mpaka kuti aume ngati chipale.
- Musaike katemera ameneyu padzuwa.
- Sungani katemera mu fuliji.

Ndondomeko zovomerezeka zomwe tiyenera kutsata pusunga timabotolo tomwe muli katemera wa I-2

Mu fuliji	Sungani kwa miyezi inayi kapena mpaka tsiku limene limaoneka pa lebulo yomwe ili pabotolopo.		
Kunja kwa fuliji		Nyengo yotentha (kutentha kopitirira 30°C)	Nyengo yofunda (kutentha kwa pakati pa 20-30°C)
	Mabotolo osatsekula	Sungani kwa masiku awiri	Sungani kwa milungu iwiri
	Mabotolo otsekula	Sungani kwa masiku awiri	Sungani kwa masiku atatu.

Chotengera chabwino cha katemera ku mudzi
(Muli nsaru yonyowetsedwa mkati)

- Katemera amakhala wosaonongeka ngati asungidwa pa malo ozizira nthawi zonse.
- Katemera amatha mphamvu akasungidwa pamalo ofunda. Simungathe kubwezera mphamvu ngakhale mutabwezera katemera m'malo ozizira.
- Sungani katemera pa malo oyenera nthawi zonse ndipo mugwiritse ntchito mwachangu katemera amene mwamuchotsa mu fuliji.

Kagwiritsidwe ntchito ka katemera wa mtundu wa I-2

- Temerani nkhuku zonse zimene zili m'kholamo. Temerani ngakhale anapiye omwe
- Donthezani dontho limodzi lakatemera m'diso la nkhuku ili yonse.
- Mudontheze m'diso limodzi lankhuku ili yonse osati m'maso onse ayi. Koma palibe choopsa chirichonse ngati mudontheza madontho opitirira limodzi m'masomo.
- Muyenera kupeleka katemerayu pa m'nthunzi.



- Kabotolo kali konse kakatemera mumakhala madontho okwana 200. Pachifukwa ichi ndiye kuti mutha kutemera nkhuku zakwana 200 pogwiritsa ntchito katemera wa m'kabotolo kamodzi.
- Pofuna kuteteza kufala kwa matenda ankhuku, musasonkhanitse nkhuku zakumadera osiyanasiyana pamene mwayamba kutemera. Muzitemera nkhuku mudzi ndi mudzi. Muonetsetse kuti mukamaliza kutemera nkhuku za mudzi umodzi, muzisamba m'manja mwanu ndi sopo musanapite kumudzi wina.
- Pamatenga mulungu umodzi kuti nkhuku zotemeredwa zikhale ndi chitetezo chokwana cha m'thupi. Ndipo chitetezo chimenechi chimatha mphamvu pakapita miyezi inayi.
- Katemerayu sioopsa. Palibe chovuta ngati anthu adya nyama yankhuku zimene zangolandira katemera posachedwapa. Palibenso bvuto lirilonse anthu kudya mazira ankhuku zomwe zalandira katemera kumene.

Mafunso omwe alimi amakonda kufunsa ndi ena mwa mayankho amene tingayankhe:

1. **Funso:** Nkhuku zanga zikufa chifukwa cha matenda achideru. Kodi mungandithandize bwanji?

   Yankho: Palibe chimene ine kapena wina aliyense angachite kuti athetse mliriwo panopa. Palibe mankhwala ochizira matenda a chideru. Panopa mungodikira mpaka nthendayi itazizira yokha ndipo akatha matendawa, muzitemera nkhuku zanu zathanzi mtsogolo muno.

2. **Funso:** Koma nkhuku zanga zili kufa. Kodi simungathe kuzitemera kuti zisiye kufa?

   Yankho: Katemera woteteza matenda a chideru simankhwala ochizira nkhuku zomwe zayamba kale kudwala kapena kufa, koma kuteteza nkhuku zomwe sizinagwidwe matendawa. Katemera sangathe kuchiza nkhuku kumatenda ngati alowa kale m'khola kapena m'mudzi. Katemera amaperekedwa kwa nkhuku za thanzi osati zimene zayamba kale kudwala chideru ayi. Palibe mankhwala ochizira matenda a chideru. Ngati chideru chagwa m'mudzi yembekezerani kuti nkhuku zambiri zikufa.

3. **Funso:** Ndilibe ndalama ndipo sindingathe kulipira malipiro a katemera. Kodi ndingachite chiyani?

   Yankho: Ngati muli ndi nkhuku zoposa khumi, gulitsani imodzi imene ingakupatseni ndalama zokwana kulipira katemera woti mutemerere nkhuku zotsalazo. Ngati simutemera nkhuku zanu, zikhoza kufa zonse ndi matenda a chideru. Pangani chiganizo choti kodi chabwino ndi chiti kukhala ndi nkhuku zisanu ndi zinayi zamoyo kusiyana ndi kuti nkhuku khumi zife.

4. **Funso:** Katemera anapha nkhuku zanga. Zinafa nditangozipatsa katemera.

   Yankho: Katemera siopsa ayi. Sangaphe nkhuku ayi. Katemera sangachite china chilichonse choononga nkhuku. Katemera amatenga mulungu umodzi kuti apereke chitetezo chokwana m'thupi la nkhuku. Ngati nkhuku zanu zinafa mutangozipatsa katemera ndiye kuti zinali zitagwidwa kale ndi matenda a chideru musanazipatse katemerayo. Ngati sichoncho, ndiye kuti nkhukuzo zafa ndi matenda ena osati a chideru ayi.

5. **Funso:** Katemera sanagwire ntchito ku nkhuku zanga. Zinafa patapita milungu ingapo nditazipatsa katemera.

   Yankho: Katemera ameneyu amagwira bwino ntchito yoteteza nkhuku ku matenda a chideru. Ngati zinafa patapita milungu ingapo mutazipatsa katemera, ndiye kuti zinafa ndi matenda ena osati chideru ayi. Katemerayu sateteza nkhuku kumatenda ena omwe amagwira nkhuku, koma a chideru nokha basi. Nkhuku zomwe zalandira katemera zitha kufa ndi matenda ena ndipo katemerayu sangathe kuziteteza kumatenda enawo.

6. **Funso:** Katemera sanagwire ntchito ku nkhuku zanga. Zinafa patapita miyezi isanu ndi umodzi nditazipatsa katemera.

   Yankho: Katemera ameneyu amagwira bwino ntchito yoteteza nkhuku ku matenda a chideru. Koma katemera sanagwire ntchito yoteteza nkhuku zanu chifukwa nthawi inakula kuchokera pamene munatemera nkhuku zanu. Katemerayu amapereka mphamvu yachitetezo kwa miyezi yokwana inayi yokha basi osati miyezi isanu ndi umodzi ayi. Nkhuku ziyenera kulandira katemera pa miyezi inayi ili yonse.

Fomu yolemba marekodi a katemera wa chitopa

Dzina la mlangizi: _____

Tsiku: _____

Dzina la Mlimi	Mudzi	Ali ndi nkhuku zingati?	Nkhuku zingati zotemeledwa?	Ndalama zapelekedwa

Fomu yodziwitsa alangizi za katemera wa chitopa*

Dzina la mlangizi: _____

Tsiku (masiku) la kutemera: _____

Mabotolo a katemera poyamba kutemera: _____

Mabotolo a katemera otsala pomaliza kutemera: _____

Mudzi	Nkhuku zingati zilipo?	Nkhuku zingati zotemeledwa?
Zonse:		

* **Mukamaliza kutemera nkhukuzo, tumizani fomu iyi kwa alangizi a za vetenari ndi alangizi ena a za ulimi.**

CHENJERANI NDI MATENDA A

CHITOPA

Courtesy of Kyeema Foundation

PELEKANI KATEMERA KU NKHUKU ZANU KUTI
MUPEWE CHITOPA

Tidzapeleka katamera wa chitopa motere:

Mudzi:	
Tsiku:	
Mtengo wankhuku imodzi:	**K10**

Zikomo